Dzina: …………………………………………………………………….. Nambala:…………………..………………..

Examination Number:……………………………

# THE CHIDIDI ZONAL EXAMINATION BOARD

## 2022 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION

# CHICHEWA

(100Marks)

**Subject Number: P032**

**Time Allowed: 2 h 15min Thursday, 28 April 1:00 – 3:15 pm**

**Dzina lanu:** ________________________________________________

**Dzina la sukulu yanu:** ________________________________________________

**Malangizo**

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi limodzi**
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi**: Gawo A, B, C** ndi **D**
3. Lembani **dzina** lanu ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba pa tsamba lino.
4. Lembani nambala ya mayeso pa mwamba pa tsamba lililonse.
5. Lembani chimangirizo chimangirizo kapena kalata mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C ndi D**
6. Muchitebulo chili pambalichi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lilikutsogolo kwake

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6-10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-20 | | | |
| 21-25 | | | |
| 26-30 | | | |
| 31-35 | | | |
| 36-40 | | | |
| 41-45 | | | |

Perekani kwa okuyanganirani kulemba mayeso (invijireta) pepala lonseli nthawi ikakwana

**© 2022 CHIZEB** **Turn Over**

Dzina: ………………………………………………………………………….. Nambala:……………………..………………..

**Langizo:** Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali mmunsiwa. Sankhani mutu wa chimangilizo **kapena** kalata. Mawu achimangilizo chanu **kapena** kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150.

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu 'Mtsinje wakwatu.' Mwa zina tsatani izi polemba

**Ndime yoyamba**

- Dzina la mtsinjewo
- Komwe mtsinjewo umapezeka
- Komwe mtsinjewo umayambira ndi kuthera

**Ndime yachiwiri**

- Zachilengedwe zina zopezeka mumtsinjewo
- Fotokozani kufunika kutatu kwa mtsinjewo

**Ndime yachitatu**

- Fotokozani zomwe mungachite pofuna kuteteza mtsinnjewo kuti usawume mtsogolomu

Kapena

**2.** Lembani kalata kwa mkulu wa zangongole, bungwe la Tukulani, P. O. Box 4, Damisoni, Ntcheu. Mumfotokozere zoti gulu lanu likufuna ngongole ya zipangizo za ulimi. Mwazina tsatirani izi polemba

Ndime yoyamba

- Cholinga cha kalata
- Malo amene gulu lanu limapezeka
- Kukula kwa gulu lanu
- Mbewu zomwe mumalima

Ndime yachiwiri

- Katundu yemwe mukufuna mugule
- Kuchuluka kwa ngongole imene mukufuna
- Kufunika kwa ngogole ku gulu lanu

Ndime yachitatu

- Njira zomwe mudzalandilire ngongole
- Njira zobwezera ngongole
- Katundu wandagwira pangongole imene mukutenga

Dzina: ………………………………………………………………………….. Nambala:…………………..………………..

**3.** Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo

Banja la a Msasa limakonda kumvera wayilesi makamaka nkhani. Madzulo ena atangomaliza kudya mgonero, bambo Msasa adauza mwana wawo Wongani kuti atsegule wayilesi.

"Mukutimva kuchokera kuno ku wayilesi ya Ululani, nthawi yakwana 7 koloko. Tikupatsirani nkhani zachitukuko wowerenga ndine Wenase kalitchi. Boma lapereka mathiredo pampu okwana 100 kwa alimi a mdera la mfumu Mtedza m'boma la Ntcheu.

Poyankhula masanawa kwa anthu omwe anasonkhana pasukulu ya Kadamsana, woyang'anira ntchito za malimidwe mdera la mbedza wati cholinga choperekera zipangizozi kwa anthu ndikulimbikitsa ulimi wothilira. Ulimi wothilira umathandiza alimi kulima mbewu zawo kangapo pachaka

Alimi a mderali awalimbikitsa kukhala m'magulu ang'onoang'ono kuti azitha kubwerekana zipangizo ndi kuthandizana. Mkuluyu watinso ngati akhala mmagulu alangizi a zamalimidwe sangavutike kuwanthandiza ndi nzeru zamakono za ulimi.

Nkhani zathera pompa. Pitirizani kumvera mapologalamu osiyanasiyana kuchokera ku wayilesi yanuyanu ya Ululani. Ndine muulutsi wanu Wenase Kalitchi."

Tsopani yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse

a. Kodi anthu adasonkhana kuti?
______________________________(2 marks)

b. Ndi ndani yemwe adatsekula wailesi madzulo?
______________________________(1 mark)

c. Kodi pologalamu ya nkhani zachitukuko idawulutsidwa nthawi yanji?
______________________________(1 mark)

d. Lembani khalidwe limodzi la banja la Msasa
______________________________ (2 mark)

e. Kodi alimi adawalimbikitsa kuti azitani?
______________________________ (2marks)

f. Fotokozani kufunika kuwiri kokhala mmagulu komwe kukupezeka mnkhaniyi
______________________________
______________________________(2marks)

g. N'chifukwa chiyani ulimi wa mthilira uli wofunika?
______________________________ (2marks)

h. Tchulani chipangizo cha ulimi chomwe chidagawidwa mwa ulele kwa alimi
______________________________(2 marks)

i. Perekani mawu ofanana mmatanthauzo ndi mawu awa:-
(i) Alimi ______________________________(1mark)
(ii) Makolo ______________________________(1mark)

j. Kodi muulutsi yemwe ali mnkhaniyi amadzitcha yani?
______________________________(2marks)

k. Perekani kufunika kuwiri kwa mtsinje pa ulimi
______________________________(2marks)

**GAWO C: Yankhani mafunso awiri (Malikisi10)**

**4.** Werengani ka nkhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

Musitafa: 'Takulandirani, masukani mkulu, tikuopeni.'

Mudyenso: 'Ife tadzera kansoti, katambala kathu ndikamene katiyendetsa.'

**Mafunso**

a. (i) Kodi malonjewa angakhale apati?

_______________________________________________ (1 mark)

(ii) Kodi Musitafa ndi yani mkankhanika?

_______________________________________________ (1 mark)

(iii) Kodi kansoti akuyimira chiyani m'nkhaniyi?

_______________________________________________ (1 mark)

b. (i) Kodi pamsewu nyali yachikasu imatanthauzani

_______________________________________________ (1 mark)

(ii) Perekani kuyipa kumodzi kwa kuba

_______________________________________________ (1 mark)

**5.** KUPANGA ZIGANIZO

*Lembani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa*

a. Chilimwe: _______________________________________________(1)

b. Zokhoma: _______________________________________________(1)

c. Kangalika: _______________________________________________(1)

d. Lende: _______________________________________________(1)

e. Sinza: _______________________________ _______________(1)

**GAWO D: (MAKISI 40)**

Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C kapenaD) mmafunso otsatirawa

**Mafunso 6 mapaka 10**:

*Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi*

**6.** Mwana <u>uyu</u> ndiwakuba

A. mlowammalo C. mneni

B. mfotokozi D. muonjezi

**7.** Patapita nthawi munthuyo <u>adadzuka</u>

A. mneni C. mfotokozi

B. muonjezi D. mperekezi

**8.** <u>Ho!</u> Zavuta kumpanda

A. mvekero C. mfuuliro

B. meni D. dzina

**9.** Mukadzawapeza <u>iwo</u> mukandiitane

A. mneni C. mfotokozi

B. mlowammalo D. muonjezi

**10.** Adapita <u>koma</u> sadzabweranso

A . muonjezi C. mlumikizi

B. mneni D. mfotokozi

**Mafunso 11 mpaka 15:**

*Perekani ntchito za maina omwe ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizozi*

**11.** <u>Chimwemwe</u> watenga zonse

A. dzina loyitanira C. pamthera nkhani

B. lolandira kathu D. mwininkhani

**12.** Mbalame yolawilira yatola <u>nyongolotsi</u>
A. mwininkhani C. pamthera nkhani
B. lolandira kanthu D. loyitanira

**13.** Fulolesi, <u>yabooka wam;mudzi</u>, watenga mimba
A. lonamizira C. dzina lapadera
B. loyitanira D. la mwinimwini

**14.** Bwera kaye kuno, <u>Thoko</u>
A. lonamizira C. loyitanira
B. lapadera D. lolandira kanthu

**15.** <u>Kumundaku</u> kwawilira
A. mtsilizi C. pamthera nkhani
B. mwininkhani D. msonyamalo

**Mafunso 16 mpaka 20**

*Sankhani magulu amayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi*

**16.** <u>Apongozi</u> anga abwera
A. mu – mi C. I – zi
B. mu – wa D. u – ma

**17.** Wapha <u>mleme</u> uja
A. mu – a C. mu – mi
B. mu – wa D. chi – zi

**18.** Nsomba ili mu <u>ukonde</u>
A. u – ma C. chi – zi
B. mu – a D. I – zi

**19.** Lolani <u>tiana</u> tidze kwa ine
A mu – mi C. u – ma
B. ku kumneni D. ka –ti

**20.** Iye adagwira <u>kumutu</u>
A. ku, kumneni C. u – ma
B. Ku, Pa, Mu D. ka – ti

**Mafunso 21 mpaka 23**

*Sankhani mitundu ya afotokozi omwe ali ndi mzere kunsi kwawo*

**21.** Dumisani ndi mnyamata <u>wamtali</u>
A. wamaonekedwe C. wa umwini
B. wamkhalidwe D. wa umwini

**22.** Dziko <u>lathu</u> ndi la mtendere
A. woloza C. waumwini
B. opatula D. owerenga

**23.** Ndi mkazi <u>wayani</u> wakuda chotere?
A. wofunsa C. wogawa
B. wamgwirizano D. wa umwini

**Mafunso 24 mpaka 25**

*Sankhani kanenedwe ka aneni ka ziganizo zotsatirazi*

**24.** Azimayi <u>khalani</u> bwino ndi ana
A. kopempha C. kachifuniro
B. kolamula D. kofotokoza

**25.** Kodi <u>watopa</u>
A. kolamula C. kopempha
B. kofunsa D. kofotokoza

**Mafunso 26 mpaka 30**

*Sankhani matanthauzo a zining'a izi*

**26.** Iye <u>wachita guni</u>
A. walephera C. wakomoka
B. walira D. wachita manyazi

**27.** Musitafa ndi <u>mthirakuwiri</u>
A. wokonda kucheza C. wokonda mabodza
B. wokonda miseche D. odanitsa

**28.** Jailosi ndi <u>kwakwatuke</u>
A. wolimba mtima C. wolemera
B. wosauka D. woyendayenda

**29.** Meka ndi <u>phungu sateya nthenga</u>
A. wokonda kudya C. wabodza
B. Wamanyazi D. womana

**30.** Sibwino <u>kulelera mwana pachinena</u>
A. kumuzuza C. Kumupusitsa
B. kumusiyitsa kuyenda D. kumuseka

**Mafunso 31 mpaka 33**

*Sankhani mayina ofanana mmatanthauzo ndi maina omwe ali ndi mzere kunsi kwawo*

**31.** Ndaona <u>kalilombe</u> lero
A. tonkhwetonkhwe C. nyani
B. pusi D. kalulu

**32.** Wapita kukatola nkhuni ku gomo

A. dondo C. phanga
B. phiri D. kutchire

**33.** Wapha zitete ziwiri

A. ziwala C. nsomba
B. zitho D. mbuzi

**Mafunso 34 mpaka 35**

*Sankhani zazimuna za zomwe zatsekedwa mzere kunsi*

**34.** Wagula thanzi

A. msoti C. chipsolopsolo
B. tambala D. nkhuku

**35.** Kwabwera ntchembere zambiri

A. ndodo C. namkungwi
B. zandonda D. zakhali

**Mafunso 36 mpaka 40**

*Sankhani mitundu ya aonjezi omwe ali ndi mzere kunsi kwawo*

**36.** Iye amaganiza mwachibwana

A. wamchitidwe C. wamuyeso
B. wanthawi D. wa malo

**37.** Musalowe muno

A. wanthawi C. wamalo
B. woletsa D. wolamula

**38.** Mutu ukundipweteka pang'ono

A. wanthawi C. wochepetsa
B. wamalo D. wamuyeso

**39.** Anagwa kasanu ndi njinga

A. wowerenga C. wamalamulo
B. wochepetsa D. wolamula

**40.** Wabwera kodi?

A. wolamula C. woloza
B. wowerenga D. wofunsa

**Mafunso 41 mpaka 45**

*Sankhani mitundu yanthambi za chiganizo yomwe yatsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi*

**41.** Sadauulure zomwe adagwirizana

A. yadzina C. yamfotokozi
B. yamuonjezi D. yamulumikizi

**42.** Ziwiri zomwe zaphedwa ndi zanga

A. ya muonjezi C. ya dzina
B. yamfotokozi D. ya m'phatikizi

**43.** Kalulu adali munthu otchuka munkhani zakale

A. ya dzina C. yoyima payokha
B. ya muonjezi D. ya mfotokozi

**44.** Ngati sadzabwera, ndikwatiwa

A. ya dzina C. ya mfotokozi
B. ya muonjezi D. yosaima payokha

**45.** Timadya kuti tikhale ndimoyo

A. ya muonjezi C. yadzina
B. yamfotokozi D. yosaima payokha

# Mayeso Athera Pamenepa